3. Kodi anthu a m'Buku Lopatulika anali kuyesa kuchita chiyani pamene anali kuchita nsembe zootcha nyama?

---

Koma Mulungu anafuna kupanga njira ina yabwino. Iye anafunanso kupanga munthu kuti akhale wabwino. Tsiku lina analankhula ndi Abrahamu nati, "Ngati udzandikhulupirira ndi kudzachita zonse zimene ndidzakuuza iwe, tsiku lina ndidzakutumizira Mpulumutsi kupyolera m'banja lako." Abrahamu anakhulupirira ndi kumumvera Mulungu. Iye anapitirizabe kuotcha nsembe kwa Mulungu. Komanso anayamba kulankhula naye.

4. Kodi Abrahamu anachita chiyani kuti Mulungu amutumizire Mpulumutsi?

---

Mulungu anasunga lonjezo lake kwa Abrahamu. Patapita zaka zambiri Mulungu anatumiza Yesu Khristu kudzafera machimo athu. Ngati timulandira Yesu, machimo athu adzakhululukidwa ndi kufafanizidwa. Choncho sitiyenera kukhala amantha ndi Mulungu chifukwa cha machimo athu. Tingathe kulankhula naye monga bwenzi chifukwa Yesu anabwera kudzatikonzera njira yabwino pakati pathu.

5. Ngati ife tisunga machimo m'mitima mwathu, kodi tingalankhule pamodzi ndi Mulungu?

---

Mabwenzi ali ndi zinthu zambiri zolankhula. Akhoza kutha nthaŵi yambiri ali pamodzi. Iwo amakonda kukhala pamodzi wina ndi mnzake. Iwo amadandaula pamene nthaŵi yolankhulira yatha. Mulungu amafuna kukhala bwenzi lathu. Iye amafuna kulankhula nafe. Iye amadandaula akamaona kuti ife sitikutha kulankhula naye. Iye amafuna kuti ife tiphunzire kupemphera bwino.

6. Kodi kupemphera ndi kutani?

______________________________________________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

5. Ayi.
1. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.
4. Iye ayenera kukhulupirira ndi kumvera Mulungu.
2. Kapena simungagwirizane nane, koma ndiganiza chinali chifukwa chakuti kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.
3. Iwo anali kupemphera.
6. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.

SABATA LACHISANU: KODI PEMPHERO NDI CHIYANI?
TSIKU LACHISANU:

Pano pali zinthu zina zimene anthu amaganizira za pemphero. Ena mwa iwo ali oona ndipo enanso mwa iwo sali oona. Lembani INDE patsogolo pa ndime iliyonse imene ikunena zoona za pemphero. Lembani AYI patsogolo pa ndime iliyonse imene ikunena zonama za pemphero.

1. Kupemphera kwabwino ndikulemekeza Mulungu chifukwa cha mphamvu yake yaikulu.

   ________________

2. Kupemphera kwabwino ndiko kungopempha zinthu zambiri zimene mukufuna.

   ________________

3. Kupemphera kwabwino ndiko kulalikira ulaliki kwa Mulungu

   ________________

4. Kupemphera kwabwino ndiko kuthokoza Mulungu chifukwa chokupatsani mwana wakhanda ndikumupempha kuti amuthandize mwanayo kuti akule bwino.

   ________________

5. Kupemphera kwabwino ndiko kumangobwerezabwereza zinthu zimene mwamva anthu ena akunena zimene zili zomveka bwino.

   ________________

6. Kupemphera kwabwino ndiko kuthokoza Mulungu chifukwa cha chakudya ndi kumupempha mvula.

   ________________

7. Kupemphera kwabwino ndiko kumvetsera kwa Mulungu kuti alankhule nanu.

   ________________

8. Kupemphera kwabwino ndiko kumuuza Mulungu za ubwino wanu.

______________________

9. Kupemphera kwabwino ndiko k,nuuza Mulungu mmene mumamukondera.

______________________

10. Kupemphera kwabwino ndiko kumuuza Mulungu kuti alange munthu wina amene akukubvutitsani.

______________________

11. Kupemphera kwabwino ndiko kumupempha Mulungu kuti akukhululukireni machimo anu.

______________________

*********************************************************

MAYANKHO.

Bwerani ndi mabuku anu ku kalasi ndipo tidzakambirana za maganizo ameneŵa.

SABATA LACHIŴIRI: KODI CHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUPEMPHERA?

TSIKU LOYAMBA:

Mphunziro ili tikufuna kuphunzira kuti, kodi ndi chifukwa chiyani pemphero lili lofunika. Pakutha kwa sabata lino muyenera kukhala okonzeka kuti mudzandiuze zifukwa zina zazikuluzikulu zimene ife tiyenera kupempherera. Anthu ena amadziŵa kuti pemphero ndiko kulankhula ndi Mulungu, komanso sapemphera. Ngati tikudziŵa zifukwa zoyenera kupemphera chingatithandize kwambiri kuchita zinthuzi bwino.

Zifukwa zake ndi izi:

(1) Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.
(2) Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amafuna chiyanjano ndi ife.
(3) Tiyenera kupemphera chifukwa ndimo mmene machimo athu akhoza kukhululukidwa ndiponso tikhoza kugonjetsera mayesero athu.
(4) Tiyenera kupemphera chifukwa ndimo mmene timasungira umoyo wathu wa uzimu.
(5) Tiyenera kupemphera chifukwa ndimo mmene timapezeramo zinthu zimene timazisoŵa.
(6) Tiyenera kupemphera chifukwa pemphero limamasula mphamvu ya Mulungu kuti igwire ntchito.

1. Kodi pali zifukwa zingati zimene tikuziphunzira?

____________________

==========================================================

Penyetsetsani bwinobwino pa ndime izi ndipo tayesani kupeza chimene ndime zonsezi zikutiuza kuti tichite.

Yesaya 55:6
Funani Yehova popezeka Iye. Itanani Iye pamene ali pafupi.

Luka 18:1:
Ndipo anawanenera iwo fanizo lakuti ayenera kupemphera nthaŵi zonse, osafooka mtima.

1 Atesalonika 5:17:
Pempherani kosalekeza.

Luka 21:36:
Koma inu khalani ochenjera, ndi kupempherera mphamvu nthaŵi zonse kuti mupyole mabvuto oyandikira kuti muimirire pamaso pa Mwana wa munthu, kuti mukalimbikike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndikuimirira pamaso pa Mwana wa munthu.

Afilipi 4:6:
Musadere nkhaŵa konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziŵike kwa Mulungu.

2. Kodi chinthu chimodzi chimene ndime zonsezi zitiuza ife kuchichita ndi chiyani?

______________________________

______________________________________________

======================================================

Akhristu amakhulupirira kuti Buku Lopatulika ndilo Mawu a Mulungu. M'Buku Lopatulika Mulungu amatiuza zimene amafuna kuti tizichita. Tiyenera kuchita zinthu zimene amatiuza zochokera m'Buku Lopatulika. Ichi chikutipatsa ife chifukwa choyamba chakuti tizipemphera.

3. Kodi ndani amene amatiuza ife kuti tizipemphera?

________________________________

======================================================

M'mudzi mwanu muli ndi ana. Inu mumaŵakonda anaŵa ndipo mumafuna kuŵaphunzitsa bwino. Mumaŵauza zinthu zimene iwo ayenera kuchita ndi zinthu zimene iwo sayenera kuchita.

4. Kodi mumayembekeza ana anu kutani pamene mwaŵauza kuti achite chinthu china chake?

______________________

Ngati tinalandira Yesu ndiye kuti ndife ana a Mulungu. Iye amatikonda ndipo amafuna kutiphunzitsa. Iye amatiuza kuti tizipemphera.

5. Kodi ndi zoona kuti tipange pemphero lokwanira chifukwa chakuti Mulungu amatiuza kuti tizipemphera?

______________________________________________

==========================================================

6. Ngati ife tili ana a Mulungu, kodi chifukwa choyamba chakuti ife tizipemphera ndi chiyani?

______________________________________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

5. Inde.
1. 6.
3. Mulungu.
6. Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.
4. Ayenera kumvera.
2. Amatiuza kuti tizipemphera

SABATA LACHIŴIRI: KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUPEMPHERA?

TSIKU LACHIŴIRI:

Dzulo tinaphunzira chifukwa choyamba chachikulu chimene tiyenera kupempherera.

1. Kodi ndi chifukwa chiyani? ______________________

______________________________________

==============================================================

Pamene tikuuza ana athu chochita timayembekezera kuti adzatimvera. Nthaŵi zina amamvetsetsa chifukwa chake chimene timafuna kuti iwo achite chinthu china, koma nthaŵi zina samvetsetsa, komabe ife timayembekezera kuti iwo amvere.

2. Monga tili ana a Mulungu, kodi tiyenera kupemphera ngakhale sitikumvetsetsa chifukwa chimene akufunira kuti tizipempherera?

______________________

==============================================================

Inde, Mulungu amayembekezera kuti tizimvera pamene Iye akutiuza kuti tizipemphera. Koma Iye safuna kuti ife tizimvera pamene sitikumvetsetsa. M'Buku Lopatulika Iye amatiuza zifukwa zambiri zimene amafunira kuti tizipempherera. Ife tifuna kuphunzira zifukwa zimenezi.

Pamene tikuuza ana athu kuti achite chinthu china, nthaŵi zambiri ndi chinthu chimene anawo amathandizidwa nacho. Komanso nthaŵi zina chingatithandize ifenso.

3. Kodi mukuganiza kuti Mulungu amatiuza kuti tizipemphera chifukwa chakuti kupemphera kwathu kumamuthandiza?

______________________________________

==============================================================

Kumbukirani kuti pachiyambi Mulungu anaganiza zopanga munthu m'chifanizo cha Iye yekha.

Genesis 1:26:

Ndipo anati Mulungu, "Tipange munthu m'chifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu..."

Taona kale kuti munthu atatha kulengedwa, Mulungu anali kubwera m'munda muja kudzalankhula naye. Kodi ichi chimatiuza chiyani za Mulungu? Kodi izi sizikusonyeza kuti Mulungu adafuna wina wake wonga ngati Iye kuti alankhule naye? Ndiganiza choncho.

4. Choncho pali chifukwa china chimene ife tiyenera kumapempherera. Nanga ndi chifukwa chanji?

__________________________________________________________

==============================================================

5. Ngati Mulungu amafuna kuti tizipemphera chifukwa chakuti pakhale chiyanjano pakati pa Iye ndi ife, nanga muganiza kuti chimachitika ndi chiyani <u>kwa Mulungu</u> ngati ife sitipemphera?

____________________________________________

==============================================================

Yakobo 4:8:

Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu.

Pano tikuona kuti Mulungu amayembekezera zambiri koposa anthu amene angopempha zinthu. Iye amafuna kuyandikana nawo ndi kuyanjana nawo.

6. Ngati muyandikira kwa Mulungu m'mapemphero, kodi Iye amachita chiyani?

__________________________________________

__________________________________________________________

==============================================================

7. Kuchokera mphunziro lathu la lero, kodi ndi chifukwa chiyani ife tiyenera kupemphera?

________________________________________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

2. Inde.
5. Mukadapereka mayankho osiyanasiyana pamenepa monga kuti Mulungu ali wachisoni kapena amasoŵa chiyanjano chathu.
1. Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.
7. Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amafuna chiyanjano ndi ife.
4. Mulungu amafuna munthu wina wolankhula naye.
6. Amabwera pafupi ndi inu.
3. Ine ndinakufunsani zimene mumaganiza, kotero kuti mayankho anu onse ali oona, koma ndikhulupirira kuti posachedwapa mudzaona kuti pemphero limathandiza Mulungu.

SABATA LACHIŴIRI: KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUPEMPHERA?

TSIKU LACHITATU:

Tsopano tili ndi zifukwa ziŵiri zimene tiyenera kupempherera. Choyamba ndi chakuti ife monga ana a Mulungu, tiyenera kupemphera chifukwa chakuti Iye amatiuza kuti tizipemphera.

1. Kodi chifukwa chachiŵiri ndi chiyani? ________________

________________________________________

==========================================

Mulungu sangofuna chiyanjano cha iye yekha. Akutipempha kuti tizipemphera chifukwa Iye amadziŵa kuti kudzatithandiza m'njira zambiri. Lero tikufuna kupeza njira zimene pemphero lingatithandizire.

2. Kodi ndani amene amathandizidwa pamene tipemphera?

________________ ndi ________________

==========================================

Werengani ndime iyi.

1 Yohane 1:9:
Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.

3. Molingana ndi ndime iyi, kodi pemphero limatithandiza bwanji?

________________________________

==========================================

Ichi ndicho chimodzi mwa zinthu zoyamba zimene tiyenera kupempha. Tisanathandizidwe ndi pemphero m'njira zina tiyenera kubvomereza machimo athu kwa Mulungu. Tiyenera kuona kuti monga tili anthu ochimwa, tili osalungama pamaso pake,

ndipo tiyenera kumpempha kuti atilungamitse.

4. Kodi pemphero limatithandiza bwanji kumachimo athu? Nanga chimachitika ndi chiyani kwa machimowo?

________________________________________

________________________________________

==================================================

Komatu Mulungu safuna kumangokhululukira machimo pamene tikuwachitabe. Iye amafuna kutithandiza kugonjetsa machimowo. Kodi mukukumbukira mmene Yesu anaŵapempherera ophunzira ake pamene anakonzekera kuŵasiya?

Yohane 17:15:
Sindipempha kuti muwachotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muŵasunge iwo kuletsa woipayo.

Patangopita kanthaŵi anauza ophunzira ake.

Mateyu 26:41:
Chezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa; mzimutu ali wakufuna, koma thupi lili lolefuka.

5. Kodi Yesu anati bwanji pouza ophunzira ake kuti akonzekere za mayesero kapena kuti kuyesedwa?

________________________________________

==================================================

Choncho tikuona kuti Mulungu amatithandiza ndi machimo mu m'njira ziŵiri. Iye amakhululukira machimo amene timaŵabvomereza pamaso pake, ndipo amatithandiza kukana kuyesedwa kumene kumatipangitsa kuti tichimwenso.

6. Kodi Mulungu tingakhale naye bwanji kuti atithandize m'njira ziŵiri zimenezi?

________________________________________

________________________________________

==================================================

7. Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kupemphera?

Tiyenera kupemphera chifukwa ndi mmene machimo athu _________________________ ndipo tikhala ndi chigonjetso cha _________________________.

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

3. Pemphero limatithandiza ife kukhala oyeretsedwa ku machimo.
5. Pakukhala maso ndi kupemphera.
7. Akhululukidwa, mayesero.
2. Mulungu, ife eni.
4. Ayeretsedwa kapena kukhululukidwa.
6. Pakupemphera.
1. Mulungu amafuna kuyanjana nafe.

SABATA LACHIŴIRI: KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUPEMPHERA?

TSIKU LACHINAYI:

Kodi mukukumbukira bwino zifukwa zimene ife tiyenera kupempherera? Kodi mungathe kuzilemba pamunsi pano? Ngati mukufuna, mungapenyerenso kumbuyo kwa masiku a 1,2, ndi 3 musanalembe.

1. Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kupemphera?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

(3) ______________________________

==========================================================

Taphunzira kuti tiyenera kupemphera chifukwa kupemphera kumatithandiza ife ku machimo athu. Koma sinjira yokhayi imene kupemphera kumatithandizira. Pali njira zina ziŵiri zimene zimapezeka pa Yohane 15. Tawerengani ndime zotsatirazi bwinobwino ndi kuona ngati mungathe kupeza zifukwa zina ziŵiri zimene tiyenera kupempherera.

Yohane 15:5-7:

> Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake, wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala zipatso zambiri, pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu. Ngati wina sakhala mwa Ine, ndiye kuti watayika kunja monga nthambi, nafota, ndipo azisonkhanitsa nazitaya kumoto, nazitentha. Ngati mukhala mwa Ine, ndi Mawu anga akhala mwa inu, pemphani chimene chilichonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu.

Poyamba taganizani za mtengo ndi nthambi zake. Ndi zokumana pamodzi, sichoncho? Kodi nthambi zingakhale ndi moyo ngati siziri zokumanizika ndi mtengo? Ayi ndithu! Yesu ananena kuti Iye ndiye mtengo, ife ndife nthambi zake.

2. Kodi tingakhale ndi moyo wa uzimu ngati sitiri wolumikizana ndi iye?

________________________________________________

==================================================

Ayi, umoyo wa Mkhristu sungapitirire ngati iye sakhala mwa Khristu. Nanga tingakhale olumikizana naye m'njira yotani? Kodi iye amapereka moyo kwa ife mwa njira yotani? Ganiziraninso za mtengo uja. Kodi mumazindikira kuti tsinde la mtengo ndi limene limapereka moyo kwa nthambi? Ilo likhoza kutero chifukwa ndi lolumikizana ndi nthambi. Khristu akhoza kutipatsabe moyo ngati tili olumikizana ndi Iye.

3. Kodi ndi njira yanji imene tingalumikizanebe ndi Khristu?

________________________________________________

==================================================

Kodi mwaona chifukwa chachikulu chimene ife tiyenera kupempherera? Ngati tipitirizabe kugwirizana ndi Khristu m'mapemphero, Iye adzapitirizabe kutipatsa moyo.

4. Kodi nchifukwa chiyani tiyenera kupitirizabe kupemphera?

________________________________________________

==================================================

Yohane 15:7:

> Ngati mukhala mwa Ine, ndi Mawu anga mwa inu, pemphani chilichonse chimene muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu.

Pano pali chifukwa china chimene tiyenera kupempherera. Chimenechi ndi chimene anthu kaŵirikaŵiri amachiganizira poyamba.

5. Monga momwe ikunenera ndime iyi, kodi chimene chimachitika ndi chiyani ngati tipempha zinthu m'mapemphero?

Limeneli ndi lonjezo lodabwitsa kwambiri lochokera kwa Mulungu. Tiyenera kupemphera chifukwa tingathe kupeza chilichonse chimene tingachifune. Mwa njira imeneyi Mulungu adzatipatsa zosoŵa zathu zonse za moyo wathu.

Koma dziŵani kuti lonjezo limeneli ndiloona pokhapokha ngati tikhaladi mwa Iye ndi Mawu ake akhalanso mwa ife. Kodi zimenezi tingatsimikize bwanji m'miyoyo mwathu? Kodi tingadzipange bwanji tokha kukhala mwa Iye ndi Mawu akenso mwa ife? Tikhoza kuchita zimenezi mwa kupemphera masiku onse.

6. Mukaganiza za izi, kodi chikuoneka kwa inu kuti tikhoza kupemphera tikakhala ndi zosoŵa ndi kuyembekeza Mulungu kutiyankha?

______________________________

==========================================================

Tisapemphere chifukwa chakuti tili ndi mabvuto okha ayi. Koma ngati tikusunga chiyanjano chathu ndi Yesu Khristu, ndiye kuti tikhoza kupemphera pamene tili ndi zosowa zathu ndipo Mulungu adzatiyankha. Ichi ndi chimodzi cha zifukwa zazikuluzikulu zimene tiyenera kupemphera.

7. Kodi ndi zifukwa ziŵiri ziti zimene tiyenera kupempherera Yohane 15:

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================

Pano tili ndi zifukwa zisanu zopempherera.
(1) Chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera
(2) Chifukwa Mulungu amafuna chiyanjano ndi ife
(3) Chifukwa ndi mmene machimo athu amakhululukidwamo ndi mmene timagonjetsera mayesero athu.
(4) Chifukwa ndi mmene timapezeramo zosowa zathu.

8. Werenganinso zifukwazi kachiŵiri. Mukatero ziphimbeni ndikuyesa kunena pa mtima zifukwa zonsezi mosaonera.

*******************************************************

MAYANKHO.

6. Ndinakufunsani maganizo anu, koma ine ndikananena kuti ayi.
4. Tiyenera kupitirizabe kupemphera kuti Iye apitirize kutipatsa moyo.
2. Ayi.
1. (1) Chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.
   (2) Chifukwa ndi mmene machimo athu amakhululukidwa ndi mmene tingagonjetsere mayesero athu.
8. Khalani okonzeka kuzinena m'kalasi.
3. Pakupemphera.
5. Anapangidwira ife.
7. (1) Tiyenera kupemphera kuti Mulungu apitirizebe kutipatsa moyo.
   (2) Tiyenera kupemphera kuti Mulungu atipatse zofuna zathu.

SABATA LACHIWIRI: KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUPEMPHERA?

TSIKU LACHISANU:

Palinso chifukwa china chachikulu chimene tiyenera kupempherera. Werengani ndime izi ndipo muyese kupeza chinthu chimene tafunsidwa kuti tizipempherera pano.

Mateyu 5:44:
Koma Ine ndinena kwa inu. Kondanani nawo adani anu ndi kupempherera iwo akuzunza inu.

Aroma 15:30-31:
Ndipo ndikudandaulirani, abale, ndi Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mzimu, kuti mudzalimbike pamodzi ndi ine m'mapemphero anu kwa Mulungu chifukwa cha ine; kuti ndikapulumutsidwe kwa osamvera aja aku Yudeya; kuti utumiki wanga wa ku Yerusalemu ukhale wolandiridwa bwino ndi oyera mtima. (Mawu olembedwa ndi Paulo).

1 Timoteo 2:1-2:
Ndidandaulira tsono, poyambayamba, kuti achitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, chifukwa cha anthu onse; chifukwa cha mafumu ndi onse akuchita ulamuliro....

Luka 10:2:
Ndipo ananena kwa iwo, "Dzinthu dzichuluka, koma antchito achepa; kotero pemphani Mwini dzinthu, kuti akankhe antchito kukututa kwake."

1. M'ndime zimenezi, kodi tikupemphedwa kuti tizidzipempherera kapena kupempherera anthu ena?

____________________

==========================================================

M'ndime zimenezi komanso malo ena ambiri a m'Buku Lopatulika ife tikupemphedwa kuti tizipempherera anthu ena. Tikupemphedwanso kuti tizipempherera adani athu, ndiponso ogwira ntchito ya Mulungu monga Paulo, ndi anthu onse. Kodi iwo tiziwapempherera chiyani? Taonani zimene Buku Lopatulika

limanena tikamawerenga m'ndime ponena zopempherera anthu onse.

1 Timoteo 2:3-4:
Pakuti ichi nchokoma ndi cholandirika pamaso pa Mulungu Mpulumutsi wathu, amene amafuna anthu onse kuti apulumuke, nafike pozindikira choonadi.

2. Tikamawerenga ndime imeneyi, kodi Mulungu amafuna kuti chizichitika ndi chiyani kwa anthu onse?

____________________________________________

==========================================================

Onaninso ndime iyi.

Luka 10:1-2:
Zitatha izi Ambuye anaika ena makumi asanu ndi aŵiri, naŵatuma iwo aŵiriaŵiri pamaso pake ku mudzi uliwonse, ndi malo aliwonse kumene ati afikeko Mwini. Ndipo ananena kwa iwo dzinthu dzichuluka, koma antchito achepa; kotero pemphani Mwini dzinthu, kuti akankhe antchito kukututa kwake.

3. Kodi ndime imeneyi akunena zokolola zanji, kapena mbewu yanji?

____________________________________________

==========================================================

M'ndime zonsezi ife tikuuzidwa kuti tizipempherera ntchito imene Mulungu amafuna kuchita yotembenuza mitima ya anthu. Koma m'chifukwa chiyani tiyenera kupemphera kwa Mulungu kuti agwire ntchito yake? Kodi sangaigwire mwa Iye yekha? Ili ndi funso lobvuta kwambiri. Sitingathe kuliyankha mwatsata-netsatane. Koma Mulungu anatiuza kuti pamene tikupemphera, mphamvu yake ili yaufulu kugwira ntchito. Ngati sitipemphe-ra, mphamvu ya Mulungu siingakhale ya ufulu kugwira ntchito. Iyi ndiyo njira imene Mulungu anapanga kuti ndi mmene zizi-khalira.

4. Mulungu amanena kuti, Iye asanagwire ntchito m'mitima ya anthu ife tiyenera ________________________

==================================================

Pano palinso chifukwa chachikulu chimene tiyenera kupemphera. Ife sitingopemphera kokha chifukwa chakuti Mulungu amafuna kuyanjana nafe kapena chifukwa chakuti ife timathandizidwa mwa ife tokha, koma tiyenera kupemphera kuti Mulungu agwire ntchito yake.

5. Kodi chimachitika nchiyani tikalephera kupempherera ntchito ya Mulungu?

________________________

==================================================

Tsopano ndikuuzeninso zifukwa zake zimene tiyenera kupemphe-rera. Muziwerenge bwinobwino ndipo muziganizire. Kenaka mupenye kumbali mosaonera papepala ndipo muyese kuzichula zifukwazo.

(1) Ife tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.
(2) Tiyenera kupemphera chifukwa Mulungu amafuna chiyanjano ndi ife.
(3) Tiyenera kupemphera chifukwa ndi mmene machimo athu amakhululukidwamo ndiponso ndi mmene timagonjetseramo mayesero.
(4) Tiyenera kupemphera chifukwa ndi mmene timasungikira umoyo muuzimu.
(5) Tiyenera kupemphera chifukwa ndi mmene timapezeramo zinthu zimene timazifuna.
(6) Tiyenera kupemphera chifukwa pemphero limamasula mphamvu ya Mulungu kuti igwire ntchito.

6. Kodi muli ndi maganizo atsopano ofotokozera kufunika kwake kwa pemphero?

________________________

==================================================